-Ife tiyenera kupita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu yekha.



PHUNZIRO LA 34

1. Kuchokera pa phiri la Sinayi, kodi Mulungu anapereka chiyani kwa a Isirayeli?
-Malamulo khumi.

2. Kodi chifukwa chiyani Mulungu yekha ndi amene ayenera kukhala Mulungu wathu?
-Chifukwa chakuti kuli Mulungu m'modzi yekha.
-Chifukwa chakuti kulibenso Mulungu wina.

3. Kodi chifukwa chiyani sitili oyenera kuti tidzipanga zinthu zomufananizira Mulungu?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.
-Chifukwa chakuti Mulungu sawoneka ngati munthu, kapena nyama kapenanso mbalame.

4. Kodi chifukwa chiyani ife tiyenera kulilemekeza dzila la Mlungu?
-Chifukwa chakuti dzina la Mulungu ndi Mulungu ndi chimodzimodzi.
-Chifukwa chakuti dzina la Mulungu ndi Mulungu ndi zimodzi.

5. Kodi chifukwa chiyani tiyenera kupuma tsiku limodzi pa sabata?
-Chifukwa chakuti Mulungu analenga dziko la pansi ndi kumwamba pa masiku asano ndi limodzi, ndipo anapuma pa tsiku lachisano ndi aŵiri.

6. Kodi chifukwa chiyani tiyenera kuti tidziŵalemekeza bambo ndi mayi athu?
-Chifukwa chakuti Mulungu anatipatsa ife bambo ndi mayi athu kuti adzitilera.

7. Malingana ndi Mulungu kodi akuti tachita chiyani tikamuda munthu wina?
-Ndiye kuti tamupha munthuyo.

8. Malingana ndi Mulungu kodi akuti tachita chiyani ngati tikumuyang'anitsitsa munthu wina, ndikumukhumbira ti-tachita naye chigololo?
-Ndiye kuti tachita naye kale chigololocho.

9. Malingana ndi Mulungu kodi akuti tachita chiyani ngati tikuganiza zakuba chinthu cha munthu wina? –Ndiye kuti tamubela kale munthuyo.

10. Malingana ndi Mulungu kodi akuti tachita chiyani ngati tikudziŵa zowona ndikulephera kunena zowonazo?
-Ndiye kuti tikunama.

11. Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuti ife tisamazifune zinthu zimene anthu ena alinazo?
-Chifukwa chakuti Mulungu mwini ndi amene wazipereka zimenezo kwa anthu enawo.

12. Kodi Mulungu akuti chiyani ngakhale titaŵamvera mal-amulo onse a Mulungu, ndikusalimvera lamulo limodzi lo-kha?
-Mulungu akulankhula kuti ndi chimodzimodzi ndi kusaŵamvera malamulo ake onse.

13. Kodi chilango chophwanya malamulo khumi a Mulun-gu ndi chotani?
-Imfa mu nyanja ya moto wosatha.

14. Kodi malamulo a Mulungu ali ngati kalilole mu njira yanji?
-Amatiwonetsa ife machimo athu.
-Amatithandiza ife kuti tidziŵawona machimo athu.



14-Ambuye anamuwuza Mose kuti, “Ndipo (Aroni) atengeko mwazi wa mwana wa mphongo wa ng'ombe, ndikuwaza ndi chala chake patsogolo pa chivundikilirocho, nawazanso mwazi ndi chala chake kasano ndi kaŵiri pasi asanafike pa chivundikilirocho.

-Kodi Aroni ankapanga chiyani ndi magazi a nyamawo?

-Ankawawaza pamwamba pa chivundikiliro cha Likasa la Chipangano.

-Kodi magaziwo anakatha kulipira machimo awo?
-Iyayi.

-Chilango cha tchimo ndi imfa, kusiyana ndi Mulungu mpa-ka kalekale ku nyanja ya moto wosatha ndipo tchimo lima-yenera kuti lidzilipiridwa lonse.

-Koma Mulungu analonjeza zodikira kaye osapereka msanga chilango ndi kuŵakhulukira akapita kwa Iye mu njira yake.

-Kodi Mulungu ankachita chiyani, Aroni akapanga zimene Iye anamulamula, kuwaza magazi a nyama pamwamba pa chivundikiliro cha Likasa la Chipangano?

-Mulungu ankadikilira kaye osapereka msanga chilango cha machimo awo kwa chaka chimodzi mpaka malipiro oy-enera atachitika.

-Ife sitingathe kumuwuza Mulungu za m'mene tinga-dzapitire kwa Iye.
-Ife tiyenera kupita kwa Mlungu mu njira imene Mulunguyo akutiwuza.

-Ife sitingathe kupita kwa Mulungu mu njira yathu.

Chipinda Chopatulikitsitsa chija kamodzi pa chaka.

Tiyeni tiŵerenge Levi 16:2

2-Ambuye anamuwuza Mose kuti," Umuwuze Aroni m'bale wako kuti asamaloŵe nthaŵi zonse ku malo opatulika kuseri kwa msaru yotchinga, ndikuchiyandikira chivundikiliro cha pa likasa, kuti angafe; popeza ndimawoneka mu mtambo pamwamba pa chivundikiliropo."

-Kodi chinakachitika ndi chiyani Aroni anakakhala kuti akumaloŵa Mchipinda Chopatulikitsitsacho m'mene ankafunira?
-Aroni anakafa.

-Aroni amaloŵa ku Chipinda Chopatulikitsitsacho kamodzi pachaka pa tsiku limene amalisankha Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Levi 16:3

3-Ambuye anamuwuzanso Mose kuti, "Umu ndi m'mene adziloŵera Aroni pa bwalo la malo opatulikalo: adziloŵa ndi ng'ombe ya mphongo ya msembe ya uchimo ndi nkhosa ya mphongo ya msembe yopsereza.

-Kodi Mulungu anamulamula Aroni kuti adzitenga chiyani, pa tsiku limene ankalisankha Mulungu kuti aloŵe Mchipinda Chopatulikitsitsacho?

-Mulungu anamulamula Aroni kuti adzitenga magazi a nyama poloŵa Mchipinda Chopatulikitsitsacho.

Tiyeni tiŵerenge Levi 16:14



15. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapereka malamulo ake?
-Kuti aŵawonetse anthu onse kuyipa kwa mitima yawo ndi machimo awo omwe.

16. Kodi ndi ndani amene angathe kuyiyeretsa mitima yathu yoyipa ndi machimoyi?
-Mulungu yekha.

-Mulungu anapereka malamulo khumi kwa a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti Mulungu sankafuna kuti a Isirayeli aŵayiwale malamulo akewo, Mulungu anaŵalemba pa mapale aŵiri a miyala.

-Mulungu anamuyitana Mose pamwamba pa phiri la Sinayi lija kuti akatenge mapale aŵiri a miyala aja.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 24:12

12-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Bwera kwa Ine ku phiri, ndipo udikilire komkuno, ndikupatsa mapale a miyala olemba maphunziro ndi malamulo kuti ndiŵaphunzitse anthu."

-Mose anamumvera Mulungu ndipo anapita pa phiri la Sinayi lija.

-Mnyamata wina wake dzina lake Yoswa anatsagana ndi Mose.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 24:13-15 ndi 18

13-Ndipo Mose ananyamuka pamodzi ndi womutumikira wake, Yoswa, chomcho Mose anakwera pa phiri la Mulungu.

14-Ndipo anaŵawuza akuluakulu aja kuti, “Mutidikilire pano, mpaka pamene tibwererepo. Aroni ndi Huli, muli nawo pompano, ndipo aliyense amene akhale ndi milandu, apite kwa iwowo.”

15-Mose anakwera mphirimo, ndipo mtambo unalivundikira phirilo.

18-Mose analoŵa mu mtambomo mpaka kukafika pamwamba pa phirilo. Anakhala komweko kwa masiku makumi anayi, usana ndi usiku.

-Pamene Mose anafika pamwamba pa phirilo, Mulungu anamupatsa iye malamulo ake khumi aja.

-Pamene Mulungu anamupatsa Mose malamulo khumi aja, Mulungu anamulamulanso Mose kuti amumangire Iye chinthu china chake.

-Mulungu anamulamula Mose kuti amumangire Mulunguyo Malo opatulika.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:8

8-Ambuye anamuwuza Mose kuti, “Ndipo mukandimangire Ine malo opatulika, kuti ndikakhale pakati pawo.”

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Mose kuti amumangire malo opatulika?

-Kodi Mulungu amasoŵa nyumba yakuti adzikhalamo?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu samasoŵa nyumba yakuti



-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anaŵawuza a Isirayeli kuti adzipha nyama chifukwa cha machimo awo?
-Mulungu ankaŵaphunzitsa a Isirayeli kuti chilango cha tchimo ndi imfa.

-Kodi Mulungu ankachita chiyani akaŵawona magazi a nyamazo?
-Mulungu akaŵawona magazi a nyamazo, ankasiya kaye osaŵapatsa msanga chilango a Isirayeli mpaka malipilo oyenerera pa machimo awowo atachitika.

-Kenako Mulungu anamulamula Mose kuti amudzodze m’bale wake, Aroni, kuti akhale wamkulu wamsembe.
-Mulungu anamulamulanso Mose kuti aŵadzodzenso ana amuna a Aroni kuti nawonso akhale amsembe.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 28:1

1-Ambuye anamuwuza Mose kuti, “Umuchotse Aroni, m’bale wako pamodzi ndi ana ake amuna, Nadabu, Abihu, Eliyazara ndi Itamara pakati pa a Isirayeli, abwere kwa iwe kuti andichitire Ine ntchito ya msembe.”

-Mulungu anamudzodza Aroni pamodzi ndi ana ache amuna kukhala amsembe.

-Koma Aroni yekha, wamkulu wa amsembe onse, ndi amene amaloredwa kuloŵa ku Chipinda Chopatulikitsitsa chija.

-Aroni anamulora kuti adziloŵa mchipindacho kamodzi pa chaka.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera, ndiponso amadana ndi tchimo lililonse, wamkulu wa a msembe, ankaloŵa ku

mikono isano, kupingasa kwake mikono isano, ndipo msikhu wache mikono itatu.

2-Ndipo ukapangenso nyanga zache pa ngodya zache zinayi; nyanga zache zikhale zoturuka momwemo, ndipo ulikute ndi mkuwa."

-A Isirayeli akachimwa, Mulungu anaŵalamula iwowo kuti adzibweretsa nyama ndipo adziyiphera pa malo opelekera msembewo okutidwa ndi mkuwa.

-Umu ndi m'mene Mulungu anaŵawuzira a Isirayeli kuti adziphera nyamazo:

Tiyeni tiŵerenge Levi 1:4

4-Ndipo ayike dzanja lache pa mutu pa msembe yopsereza; ndipo idzalandiridwa mmalo mwache, kukhala yomupepesera iye.

-Mulungu anamulamula mu Isirayeli kuti akafuna kupha nyama, adziyika dzanja lake pa mutu wa nyamayo, ke-nako adziyipha.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti akafuna kupha nyama, adziyika manja awo pa mutu wa nyama imene akufuna kuyiphayo?

-Mu Isirayeli ankayika dzanja lake pa mutu wa nyama imene ankafuna kuphayo, kuwonetsa kuvomereza pa maso pa Mulungu kuti iyeyo wachimwa ndipo akuyenera kufa, koma Mulungu wavomereza imfa ya nyama kuloŵa m'malo mwa munthuyo.

-Kodi magazi a nyama anakatha kulipila pa machimo a a Isirayeli?
-Iyayi.



adzikhalamo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amakhala paliponse pa nthaŵi zonse.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Mose kuti amumangire malo opatulika Iye?

-Kodi mukulikumbukira lonjezo limene anapereka Mulungu kwa a Isirayeli?

-Kodi Mulungu anapereka lonjezo lotani kwa a Isirayeli?

-Kodi Mulungu anati kuti achita chiyani, a Isirayeli akaŵamvera malamulo ake onse?

-Mulungu analonjeza zakuti aŵadalitsa a Isirayeli akaŵamvera malamulo ake onse.

-Kodi Mulungu anaŵawuza a Isialayeli kuti Iye adzachita chiyani ngati a Isirayeliwo saŵamvera malamulo Ake on-se?
-Mulungu anakaŵapatsa a Isirayeli chilango anakakhala kuti saŵamvera malamulo ake onse.

-Kodi a Isirayeli anakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anadziŵa zakuti a Isirayeli satha kuŵamvera malamulo ake onse?
-Inde.

-Kodi chilango cha anthu amene akuphwanya lamulo nga-khale limodzi la Mulungu ndi chotani?
-Imfa mnyanja ya moto wosatha.

-Ichi ndi chifukwa chake Mulungu anamulamula Mose kuti amumangire malo opatulika.

-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵakonda a Isirayeli kwambiri, Iye sanafune kuti a Isirayeliwo akhale mnyanja ya moto wosatha.

-Chifukwa chakuti Mulungu sanafune kuti a Isirayeli akhale mnyanja ya moto wosatha, Mulungu anapereka njira yakuti apulumukire a Isirayeli.

-Iyi ndiye njira imene anapereka Mulungu kwa a Isirayeli:

-A Isirayeli akachita tchimo ndi kuphwanya limodzi mwa malamulo a Mulungu aja, a Isirayeliwo ankapita ku malo opatulika aja atatenga magazi a nyama.

-Kodi Mulungu ankachita chiyani akaŵawona magazi a nyamawo?
-Mulungu akaŵawona magazi a nyamawo, Iye ankasiya kaye osaŵapatsa chilango a Isirayeli mpaka malipiro oyenelera atachitika.

-Kodi Mulungu anafuna kuti Mose amange bwanji malo ake opatulika aja?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:9

9-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Mukamange kachisi opatulika ndi zonse za mkati mwake ngati m'mene ndikuwuzireni kapangidwe kake."

-Kodi Mulungu ankafuna kuti Mose ndi a Isirayeli amange bwanji malo opatulikawo?
-Ngati m'mene anamulamulilira Mulungu.



31-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Ukawumbe nsaru yotchinga ya thonje la madzi, lofiirira ndi lofiira, la bafuta wa thonje labwino kwambiri, ukapetere limodzi ndi akerubi ndipo tchitoyo yigwiridwe ndi mmisiri.
33-Ndipo ukakoleke nsalu yotchingirayo pa zokowerazo, nuloŵetse likasa la Mboni kuseli kwa nsalu yotchingirayo. Ndipo nsaru yotchingirayo, idzakugaŵirani pakati pa malo opatulika ndi opatulikitsitsa."

-Kodi tanthawuzo la nsaru yogaŵa pakati pa Chipinda Chopatulika ndi Chipinda Chopatulikitsitsa ndi lotani?

-Nsaruyo imaŵakumbutsa a Isirayeli kuti ali osiyidwa ndi Mulungu chifukwa cha machimo awo.

-Tchimo limasiyanitsa Mulungu ndi anthu ngati m'mene yinkasiyanitsira nsaru ija pakati pa Chipinda Chopatulika ndi Chipinda Chopatulikitsitsa.

-Atatha kuyika nsaruyo, Mulungu anamulamula Mose kuti ayike Likasa la Chipanganolo M'chipinda Chopatulikitsitsamo.

-Mulungu anamulamulanso Mose kuti amange mpanda wozungulira malo opatulikawo.
-Mkati mwa mpandamo, kumaso kwa malo opatulikawo, Mulungu anamulamula Mose kuti amange guwa la msembe lopangidwa ndi mitengo yabwino kwambiri yokutidwa ndi mkuwa.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 27:1-2

1-Ambuye anamuwuzanso Mose kuti, "Ndipo upange guwa la msembe la mtengo wa sitimu, utali wache

chivundikilirocho.

-Mulungu anamulamula Mose kuti apange kerubi wina ku mbali imodzi ya chivundikilirocho, kerubi wina akhale ku mbali ina ya chivundikiliro cha Likasa la Chipanganolo.

-Mulungu analamula kuti akerubiwo adziyang'anana, ndipo afunyulire mapiko awo m'mwamba kuti adzipereka nthuzi pa chivundikiliro cha Likasa la Chipanganolo, nkhope zawo zitayang'ana pasi pa chivundikilirocho.

-Kenako Mulungu anamulamula Mose kuti ayike chivundikilirocho pamwamba pa Likasa la Chipanganopo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:21-22

21-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Ukayike chivundikilirocho pamwamba pa likasalo, ndi kuyikamo Mboni imene ndidzakupatseyo mu likasamo.
22-Ndipo pomwepo ndidzakumana ndi iwe, ndi kulankhula ndi iwe, ndiri pamwamba pa chivundikilirocho, pakati pa akerubi aŵiriwo okhala pa likasa la Mboni, ndipo ndidzakupatsa malamulo a ana a Isirayeli.

-Mulungu anamulamula Mose kuti ayike mkati mwa Likasa la Chipanganolo mapale aŵiri a miyala amene Mulunguyo analembapo malamulo khumi aja.

-Ulemelero wa Mulungu udzakhala ndi a Isirayeli pamwamba pa chivundikiliro cha Likasa la Chipanganolo.

-Mulungu anamulamulanso Mose kuti ayike nsaru yotchinga (yogaŵa) pakati pa Chipinda Chopatulika ndi Chipinda Chopatulikitsitsa.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 26:31 ndi 33



-Ngati m'mene Mulungu anamulamulilila Nowa kapangidwe ka chombo, chomchoso Mulungu anamulamulila Musa kuti amange malo opatulikawo ngati m'mene anamuwuzira Mulungu.

-Ife sitingathe kumuwuza Mulungu m'mene tingafikire kwa Iye.
-Ife tingathe kufika kwa Mulungu kupitira mu njira imene Iye angatiwuze.

-Ife sitingathe kupita kwa Mulungu kupitira mu njira yathu.
-Ife tiyenera kupita kwa Mulungu kupitira mu njira ya Mulungu yekha.

-Kodi timaphunzira kuti za njira ya Mulungu?
-M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Kodi Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti amange ndi chiyani malo opatulikawo?
-Zikopa za nyama ndi zinthu zina zopangidwa ndi ubweya wa mbuzi.

-Kenako Mulungu anamulamula Mose kuti amange zipinda ziŵiri mkati mwa malowo.

-Chipinda choyamba chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulika.
-Chimenechi chinali chipinda cha Mulungu.

-Anthu ochepa okha ndi amene ankaloledwa kuloŵa mchipinda choyambachi.

-Chipinda chachiŵiri chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulikitsitsa.
-Chipinda chimenechi chinali cha Mulungu yekha.

-Munthu m'modzi yekha ndi amene ankalowâ ku Chipinda Chopatulikitsitsachi kamodzi pa chaka.

-Izi zinkakhala chomchi chifukwa chakuti ulemelero wa Mulungu unkakhala M'chipinda Chopatulikitsitsachi.

-A Isirayeli anakamanga malo opatulikawo malingana ndi m'mene Mose anaŵawuzira, ndiye kuti ulemelero wa Mulungu unakalowâ Mchipinda Chopatulikitsitsacho.

-Kenako Mulungu anamulamula Mose kuti apange chinthu chakuti achiyike M'chipinda Chopatulikitsitsacho.

-Chinthucho chinkatchedwa kuti Likasa la Chipangano.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:10-11

10-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Ndipo ukapange likasa la mtengo wa sitimu. Utali wache, mikono iŵiri ndi theka, kupingasa kwache, mkono ndi theka, msinkhu wache, mkono ndi theka.
11-Ndipo ulikute ndi golide wabwino kwambiri, ulikute mkati ndi panja, ndipo ulipangire mkombero wa golide kuzungulira lonselo."

-Mulungu analamula kuti Likasa la Chipanganolo lipangidwe ndi mtengo wabwino kwambiri.

-Mulungu analamulanso kuti Likasa la Chipanganolo likutidwe ndi golide.

-Mulungu analamulanso kuti Likasa la Chipanganolo likhale mikono iŵiri ndi theka, utali wache, mikono iŵiri ndi theka, kupingasa kwache ndi mkono ndi theka msinkhu wache.



-kenako, Mulungu anamulamula Mose kuti apange chivundikiliro cha Likasa la Chipanganolo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:17

17-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Ukapangenso chivundikiliro cha golide wabwino kwambiri , chikakhale mikono yiŵili ndi theka utali wache, mkono ndi theka kupingasa kwake.

-Mulungu analamula kuti apange chivundikiliro cha Likasa la Chipanganolo cha golide weniweni.

-Mulungu analamula kuti chivundikilirocho chikhale mikono iŵiri ndi theka utali wache, mkono ndi theka kupingasa kwache.

-Pamwamba pa chivundikilirocho ndi pamene udzikhala ulemelero wa Mulungu ndi a Isirayeli.

-Kenako Mulungu anamulamulanso Mose kuti apange akerubi aŵiri a golide amene akhale pamwamba pa chivundikilirocho.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 25:18-20

18-Ambuye anamuwuza Mose kuti, "Ukapangenso akerubi aŵiri a golide; uwasule mapangidwe ache, pa mathungo ache aŵiri a chivundikilirocho.
19-Ndipo upange kerubi m'modzi ku thungo lina, kerubi wina ku thungo lina; upange akerubi ochokera ku chivundikilirocho, pa mathungo ache aŵiri.
20-Ndipo akerubi afunyulire mapiko awo m'mwamba , ndi kuphimba chivundikilirocho ndi mapiko awo, ndipo nkhope zawo zipenyane; nkhope za akerubu zipenye ku